UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NTCHEU M'DZINJA LA 2024-2025

DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wocheperako mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025. Boma la Ntcheu likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika, komanso oposerapo. Pali kuthekera kolandira mvula yochulukirapo m'mwezi wa February 2025 kuposa mwezi wa February chaka chatha.

October 2024



M'mwezi wa October, Boma la Ntcheu likuyembekezera kulandira mvula ya mulingo okhazikika wa pakati pa 0mm ndi 30mm.
Mvula yoyambilira itha kudzabwera ndi mphepo yamkuntho komanso ziphaliwali

November 2024



Mmwezi wa November, madera a TA Njolomole akuyembekezera kulandila mlingo wa mvula odutsa 100mm. Madera ambiri a bomali adzalandila mvula pakati pa mulingo wa 20mm and 50mm. Mvula yobzalira ikuyembekezereka kudzayamba pakati pa sabata lomaliza la mwezi wa November ndi sabata loyamba la mwezi wa December.

December 2024



Madera a kumwera cha kuzambwe kwa TA Njolomole ndi madera ozungulira pa Ntcheu Boma akhoza kudzalandira mvula yoposera 200mm. Komabe madera ambiri akuyembekezera kulandira mvula ya pakati pa 100-160mm

January 2025



mvula yochulukilapo ya mlingo odutsa 250mm ikuyembekezeleka kugwa madela ambiri m'bomali monga madela a TA Njolomole, Ntcheu Boma ndi kumwera chakuzambwe kwa TA Mpando. Mvula yokwana mulingo wa 150mm ikuyembekezereka kugwa madera ozungulira SC Champiti.
Pali kuthekera kodzakhala ndi Ng'amba yosadutsa sabata imodzi.

February 2025



Mulingo wa mvula wokhazikika ndiponso kuposerapo ukuyembekezereka kugwa madera ambiri pa mlingo wa pakati pa 200-250mm. Koma madera ena ozungulira SC Makwangwala, adzalandira mvula yokwana 150mm.
Pali kuthekera kwakukulu kodzakhala ndi ng'amba yosaposera sabata imodzi.

March 2025



Mvula yopitilira 240mm ikuyembekezereka mmadera a SC Champiti ndi ku mpoto cha kumvuma kwa TA Phambala pomwe madela ena otsalawo adzalandira mvula ya mlingo wa pakati pa 110 ndi 150mm

April 2025



Dzinja likuyembekezereka kufika kumathero mu sabata ya chiwiri ya April ndipo madela ambiri m'bomali adzalandila mvula ya mlingo pakati pa 20mm ndi 70mm.

Boma la Ntcheu likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika, komanso oposerapo koma pali kuthekera kolandira mvula yochulukirapo m'mwezi wa February 2025 kuposa mwezi wa February chaka chatha. Mvula yodzalira ikhoza kuyamba pakati pa sabata yomaliza ya November ndi sabata loyamba la December. Mathero a mvula akuyembekezereka sabata yachiwiri mpaka sabata yachitatu ya April 2025. Dzinja lonse likuyembekezeleka kukhala la masiku 120 mpaka 150. Chiopsezo cha ng'amba yosaposera sabata imodzi mu January ndi February 2025.
Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.

NTCHEU			
MONTH	NORMAL RANGE		FORECAST
OCT	4	29	10
NOV	52	72	57
DEC	147	263	207
JAN	219	315	344
FEB	198	261	255
MAR	149	190	201
APR	14	40	56



Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024

Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com